NYA_TTB_0940_20161104**_script**

**Danieli : 10:11-21**

**Mutu : M'thengawa Kumwamba**

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni lero tiyambe ndi mau apa Hoseya 6:1-2, amene akuti, "Tiyeni, tibwerere kunka kwa Yehova, pakuti wang'amba, nadzatipoletsera; wakantha, nadzatimanga. Atapita masiku awiri adzatitsitsimutsa, tsiku lachitatuadzatiutsa; ndipo tidzakhala ndi moyo pamaso pake."

Mupologalamu yatha tinali kukambirana pa Danieli 10:1-10, pamene timasanthula za ulosi wa Danieli umene ukuonetsa Kristu muulemererо wake. Ndipo lero pa Danieli 10:10-21, tiunika za m'thengawa Kumwamba.

**Danieli 10**

10. Ndipo taonani, linandikhudza dzanja ndi kundikhalitsa ndi maondo anga, ndi zikhato za manja anga.

Danieli akanali ndi mantha akuru, koma tikuona kuti ayankhidwabe ndi kulimbikitsidwa ngakhale akupezabe zobvuta

kuti mantha achoke.Koma tamvani mngelo, amene ndikukhulupirira kuti ndi Gabrieli chifukwa ndiye wakhala akutumikira nthawi zina, akunena kuti Danieli ndiye wokondedwa ndi Mulungu.Ndiye pakumukhudza Danieli, mngelo akumuuza kuti, ayenera kutcherakhutu ndi cholinga chakuti amvetsetse mau ake.Pachifukwa chimenechi, mngelo akumuuza Danieli kuti aimirire kuti akhozekumvetsera bwino.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna tinenetse kuti, mphamvu ndi chitonthozo, zimadzapang'onopang'onokwa iwo amene athedwa nzeru chifukwa chamaonekedwe komanso liwu la Kristu. Kutanthauza kuti ndi anthu othedwa kapena wodzichepetsa wokha, ndiwo amene Mulungu amawadzutsapang'onopang'ono kufikira ataimirira.Awa, ndiwo mau amene adanena mneneri Hoseya 6:2, amene anati, "Atapita masiku awiri adzatitsitsimutsa, tsiku lachitatuadzatiutsa; ndipo tidzakhala ndi moyo pamaso pake."

Nkhani ikuti inu ndi ine, tonse ndife anthu olephera, kotero kuti tifunadi Mulungu kuti azitigwira dzanja nthawi yonse kuti tikhale ndi moyo.Pachifukwa chimenechi, sitiyenera kunyoza kapena

kuderera tsiku momwe mukuoneka kuti zinthu zazing'ono zikuchitika, chimene ndicho chiyambichoonetsa chifundo cha Mulungu.

11. Nati kwa ine Danieli, munthu wokondedwatu iwe, tazindikira mau ndirikunena ndi iwe, nukhalechiriri; pakuti ndatumidwa kwa iwe tsopano. Ndipo pamene adanena mau awa kwa ine ndinaimirira ndi kunjenjemera.

Mu verse 10, Danieli akunena kuti dzanja lidamukhudza ndipo anauka kotero kuti anakhala pazikhatho ndi maondo ake.Kutanthauza kuti Danieli anali atadzuka, koma anali kutsamira pa manja ndi maondo, kukhala ngati nyama ikuima pa miyendo inayi. Ndiye tikunena kuti ngati masomphenya ena aja anali kuonetsa Kristu, apatiri ndi umboni wonse kuti uyu, anali mngelo Gabrieli. Tsono mngelo uyu, pano wadzutsa Danieli ndipo akumuitanira dzina lakuti, "munthu wokondedwa."

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti ngakhale Mulungu anakonda dziko lonse, monga mwa mau aja apa Yohane 3:16, akuti anatuma Mwana wake ngati Mpulumutsi wa dzikoli, koma tiyenera kudziwa kuti alipo anthu ena, amene

amakondedwakwambiri chifukwa cha ubale wawo wapadera ndi Mulungu wawo. Kutanthauza kuti chiyanjano chanu ndi Mulungu ndicho chimene chimapanga ubale wapadera ndi Mulungu.

Taonani tiri ndi Davide, amene anakondedwamwapadera ndi Mulungu monga mwa Machitidwe Atumwi 13:22, amene akutsimikizadi kunena kuti, “Ndipo m’mene atamchotsa iye, anawautsira Davide akhale mfumu yawo, amenensoanamchitira umboni, nati, ndapeza Davide mwana wa Jese, munthu wa pamtima panga, amene adzachita chifuniro changa chonse.” Komanso tiona Mtumwi Yohane 13:23, akunena kuti, “Koma m’modzi wa akuphunzira ake, amene Yesu anamkonda, analikutsamira pa chifuwa cha Yesu.” Nkhani ikunena kuti inu ngati kholo, mumakonda ana anu onse, koma alipo mwana wina amene mumamkondamwapadera mosiyana ndi ena onse, momwemonso mtima wa Mulungu umakhala paubale wapadera ndi iwo amene amukonda Iye, kwambiri.

Tere, pano tikuona mngelo akumutsutsa Danieli ndi kumulimbikitsa kuti amvetse Uthenga umene anadza nawo kwa iye. Ndimau amenewa Danieli wadzuka ndipo waimirira ngakhale

kuti anali kunjenjemera. Uthenga wa mngelo uja, unali wofuna kumulimbikitsa Danieli popeza chifuniro cha Mulungu pomupatsa masomphenya amenewa, chinali kufuna kuonetsa kuti Mulungu anali wachifundo ndi chikondi kwa iye, kotero kuti Danieli samayenera kudera nkhawa ayi. Kutsimikiza mau aja akuti, ngati Mulungu ali ndi ife, adzatikaniza ndani?

Ndiye tikuphunzira kuti palibe ulemu umene ungaperekedwekwa munthu, woposa umene Danieli analandira kwa mngelo wa Mulungu kuti anali wokondedwa ndi Mulungu. Zonsezi zikuchitika chifukwa cha kudzichepetsa kwa Danieli, kulapa machimo akekawiri-kawiri, chikondi chake cha pa anthu ake, kukhala ndi chilakolako chofuna kudziwa za m'Mwamba komanso kupirira kwake pofuna nkhope ya Mulungu. Izi, ndizo zimene zinapangitsa kupeza chifundo ndi chikondi chapadera chochokerakwa Mulungu. Tere, ndizo zimene zimaonetsedwakwa anthu omwe amadziona kuti ndi wosayenera.Kodi inu mumadziona motani pamaso pa Mulungu?

Panonso ndifuna muone kuti kuyambira tsiku lomwe anayamba kusala ndi kupemphera, pemphero lake linamveka kotero kuti

mngelo anauzidwa kupita kwa Danieli ndi kukamuthandiza. Tsono mwina inu mukufunsa kuti chifukwa chiyani Danieli wokondedwa ndi Mulunguyo anadikirakwamasabata atatu asanalandire yankho? Yankho likuti, Mulungu amachita zinthu zake zonse panthawi yake, kotero kuti zikutsimikiza kuti ndiye Mulungu wadongosolo. Ndiye tikunena kuti ngati Danieli, amene anali wokondedwa wake wa Mulungu, akhoza kudikiramasabataatuwa, kodi chingalepheretse ife kuchita chomwechi m'chiyani? Nkhani ikuti inu ndi ine, sitiyenera kuchita mopupuluma ayi, chifukwa Mulungu ali ndi nthawi yochitira chinthu chirichonse ndipo simungamulamule kuchita monga inu mufuna ayi.

12. Pamenepo anati kwa ine, usaope Danieli; pakuti kuyambira tsiku loyamba lija unaika mtima wako kuzindikira ndi kudzichepetsa pamaso pa Mulungu wako, mau ako anamveka; ndipo ndadzera mau ako.
13. Koma kalongawa ufumu wa Peresiya ananditsekerezera njira masiku makumi awiri ndi limodzi; ndipo taonani Mikaeliwina wa akalonga omveka, anadza kundithandiza; ndipo ndinakhalakomweko ndi mafumu a Peresiya.

Danieli pano akulimbikitsidwa kuti samayenera kuchita mantha ndi kudza kwam'ngeloyo komanso samayenera kudankhawa chifukwa chakuti mapemphero ake anali asanayankhidwe.

Wokondedwa anzanga apaulendo, apa ndipo pamene anthu ambiri timataya chikhulupiriro chathu komanso mwayi wakuti tilandire yankho kuchokera Mulungu. Ndikunena kuti ambiri a ife, timataya mtima kapena chikhulupiriro msanga mwa Mulungu, pamene tiona kuti sitikuyankhidwa monga ife tifuna. Koma ndifuna tiphunzire kudzera kwa Danieli kukhala ndi mtima wopirira ndi kudikira kuti chifuniro cha Mulungu ndicho chichitike basi. Mwanjira ina tikunena kuti, inu ndi ine, tiyenera kukhala nawo mtima wa Kristu, womwe adauonetsa pa Luka 22:42, pamene anapemphera kuti, "Atate mukafuna Inu, chotsanichikho ichi pa Ine; koma si kufuna kwanga ayi, komatu kwanu kuchitike." Kodi inu muli nawo mtima wodikira kapena kuyembekezera pa Ambuye?

Tsono zikuonetsa kuti Danieli anapereka nkhope yake kwa Mulungu kwa masabata atatu, akufunitsitsa kudziwa zatsogolo kapena za kumasulidwa kwa anthu ake, komanso amafuna kudziwa za udindo wake pantchito imeneyi ndi njira yomwe

angagwiritse ntchito paudindowakewo. Ndiye mngelo akumuuza kuti, iye wadza kwa Danieli ndi cholinga chofuna kumudziwitsa ndi kumulimbikitsa kuti kuyambira tsiku lomwe adayamba kufufuza za chinthu chimenechi, pemphero lake,linamveka. Tsono mngelo akunena kuti, panali cholinga chimodzi kuti yankho la pemphero lake lisaperekedwe mofulumira, Mulungu anali kufuna kuti Danieli adziwe kuti pemphero lake linayankhidwa kale, koma pamafuna kuti adzichepetse ndi kudzizunza yekha pamaso pa Mulungu. Awa, ndiwo mau amene akutsimikiza kuti yankho la pemphero lathu, limakhala litaperekedwa kale, koma losatumizidwapachifukwa china chodziwa Mulunguyo, koma osati kuti silinamveke ayi.Tikunenetsa kuti pemphero lanu linayankhidwa kale, ngakhalekuti papita nthawi yaitari, koma yankho limakhala kuti likubwera ndi mthenga wake. Mwanjira inatikunenetsa kuti inu, simuyenera kutaya mtima chifukwa chakuchedwaku.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndikutsindika pano kunena kuti Danieli akanadziwa kuti mngelo anali mnjirakudzapereka yankho ndi kumulimbikitsa, akanamasulakusala kwake. Uthenga ukunena kuti inu ndi ine, m'nthawi yamasautso, momwe tikuona

ngati kuti mapemphero athu sakufika Kumwamba, pamene chinthu chomwe tikupemphererasichikuyankhidwa, pamene anzathu kapena ana athu sakutembenuka mtima, pamene chipembedzo chikuchuluka pakati pa wopembedza, pamene mabvuto sakutisiya, Mulungu akunena kuti tikanadziwa kuti yankho la pemphero lathu, lili panjira likudza ndi mngelo, mitima yathu ikanakondwera komanso misozi ikanachoka. Mwanjira ina Uthenga ukuti, inu ndi ine, sitiyenera kudera nkhawa, pamene tipemphamoona mtima, tiyenera kukhala ndi chitsimikizo chakuti yankho la pemphero lathu likubwera ndipo lifika nthawi ina iliyonse. Kutsindika kunena kuti, kodi ife tiri ndi bvuto lanji m'nthawi yosautsa ngati ino, kuti tisakhulupirire Mulunguamene alipoamene akumva ndi kupereka yankho kupemphero lathu?

Tsono munkhani yonseyi tikupeza kuti palibe mayi, amene ali ndi chikondi pa mwana wake, monga chomwe chaonetsedwa ndi mngelo kumutonthozaDanieli pamene anali ndi mantha. Ndiye Uthenga ukuti, iwo amene amakondedwa ndi Mulungu, alibe chifukwa chakuti aope choipa, popeza mtendere ndiwawo. Kutsindika kuti Mulungu mwa mau ake, amalonga moyo mwa

anthu ake, kotero kuti amatumaangelo ake ndi kupereka mtendere kwa ana ake. Komanso tikunena kuti pamene tizindikira zomwe Mulungu achita ndi ife, ndinjira zomwe akuzigwiritsa ntchito, ife sitidzachokapankhope yake ndipo tidzakhalabe paubale wabwino ndi Iye.

Tsono ndikoyenera kuona nkhani iyi, mugawo lakuti pamene mngelo akudza kwa Danieli, akuonetsa kuti mumlengalenga muli nkhondo. Tikunena kuti m'dziko lomwe ifesitiliona muli nkhondo kapena kulimbana pakati pa chabwino ndi choipa, kuwala ndi m'dima, pakati pa Mulungu ndi satana. Taonani pamene mngelo akumuuza Danieli kuti kuyambira tsiku lomwe anapereka pempho lake iye anali panjira kupita ndi yankho, koma panjiraanatsekerezedwa. Ichi, ndichifukwa chake Paulo pa Aefeso 6:11-12, adanena kuti, "Tabvalanizida zonse za Mulungu kuti mudzakhoza kuchirimikapokanamachenjereroa mdierekezi. Chifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nawo mwazi ndi thupi, komatu nawo maukulu ndi maulamuliro ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi auzimu a choipa m'zakumwamba."

Nkhani ikuti pali kusiyana kwa maudindo ya mphamvu za satana. Tere tikunena kuti mphamvu zimenezi ndizo zimene zikhoza kuchedwetsa yankho la pemphero lanu. Mwanjira ina tikunena kuti pemphero ndilo kumenya nkhondo yauzimu nthawi yonse. Ichi, ndichimene Paulo pa Aroma 15:30, adanena kuti, “Ndipo ndikudandaulirani, abale mwa Ambuye wathu Yesu Kristu, ndi chikondi cha Mzimu, kuti mudzalimbike pamodzi ndi ine m’mapemphero anu kwa Mulungu chifukwa cha ine.”Kutanthauza kuti Paulo anali kuwalimbikitsa akristu aku Roma kumenya nkhondo yauzimumogwirizanandi iye.

Mwachisoni masiku ano, kuti mapemphero ena amachitika mwachizolowezi komanso mopepuka kwambiri.Lero anthu amaona ngati kulankhula mau okoma ndi omveka bwino, ndiko kumenya nkhondo ndi satana, ayi sichoncho.Chifukwa asirikari akakhalapankhondo palibe kupukutamfuti.

Tsono nkhondo iyi, ndi yomwe mngelo adamuuza Danieli, pamene adati, “Koma kalongawa ufumu wa Peresiya ananditsekereza njira masiku makumi awiri ndi limodzi.” Ndiye funso likuti, kodi ndani amene adamutsekereza? Yankho likuti munthu wa padziko

sangathe kuchita chimenechi, koma ndi atumiki a satana. Kutsimikiza kuti Mulungu ali ndi angelo ake, pamene satana alinso ndi ake, awa ndiwo amakhala pankhondo nthawi yonse. Tsono pamene tifuna chifukwa chomwe mngelo adatsekerezedwera, Danieli adzatipatsa yankho lokhudzana ndi ufumu wa Peresiya ndi Greece. Koma akunena kuti mngelo Wamkulu Mikaeli anadza kudzamulimbikitsapankhondi ya Peresiya.

Pachifukwa ichi, tikunenetsa kuti moyo wachikristu ndiwo udindo waukulu, umene umasiyana ndizomwe tikhoza kunyamula pathupi *lathu.

14. Ndadzera tsono kukuzindikiritsachodzagwera anthu a mtundu wako masiku otsiriza; pakuti masomphenyawo ndiwo a masiku a m'tsogolo.

Danieli ndiye munthu amene wakhala akufufuza kuti adziwe zinthu zina zobisika.Ndiye Danieli anadzala ndi chimwemwe pamene mngelo anamuuza kuti wadza kudzamuuza chinthu chomwe chidzachitika m'tsogolo. Kunena kuti Danieli amafunitsitsa kudziwa chomwe chidzachitika kwa anthu ake, m'masiku otsiriza a mpingo pamene ulosi uwu, udzakwaniritsidwa pamene nthawi inali

kuyandikirakudza kwa Mesiya. Ndiye Danieli akuuzidwa kuti masomphenyawaadzatenga masiku ambiri asanakwaniritsidwe kufikira muulamuliro wa wokana Kristu womwe, unaonetsedwa ndi ulamuliro wa Antiokasi. Tere Habakuku 2:3, akunenetsa kuti, “Pakuti masomphenyawo alindira nyengo yoikidwiratu, ndipo afulumirirapotsirizira pake, osanama; akachedwauwalindirire; popeza afika ndithu, osazengereza.”

15. Ndipo atanena ndi ine monga mwa mau awa, ndinaweramitsa nkhope yanga pansi ndi kukhala du.
16. Ndipo taonani, wina wakunga ana a anthu anakhudza milomo yanga; pamenepo ndinatsegula pakamwa panga ndi kunena naye woimapopenyananane, Mbuye wanga, chifukwa cha masomphenyawo zowawa zanga zandibwerera ndipo ndiribenso mphamvu.

Pano Danieli wathedwa nzeru ndi zomwe zalankhulidwakwa iye. Taonani momwe pemphero lake layankhidwira, mwina layankhidwa ndi mosiyana ndi zimene iye anali kuganiza. Komanso taonani kupezeka kwa mngelo, ndi maonekedwe okongola aulemerero wake. Zonsezi zapangitsa kuti Danieli athedwe nzeru. Ndiye funso likuti,

kodi inu mukhoza kulimbaosagwa pansi mutaona mngelo wa Mulungu akukufotokonzerani zomwe zidzachitika ku banja lanu, kwa abwenzi anu ngakhalenso kudziko lanu?

Ndiye mngelo uja, amene tikukhulupirira kuti anali Gabrieli, akukhudza pakamwa pa Danieli. Kutanthauza kuti anali kumupatsa mphamvu kuti akhoza kulankhula zomwe zinaululidwakwa iye. Apa, ndipo pamene mantha ake anamuchokera, kotero kuti ndipo pamene anayamba kulankhula ndi mngelo uja.Koma pamene anaona mngelo uja, anaona zoipa zake, kotero kuti anachita manyazi ndi kusoweka mphamvu.Umu, ndimomwe amachitira Mulungu kuti amagwiritsa ntchito zipangizo zopanda mphamvu ndi zonyozeka. Kutanthauza kuti Mulungu amagwiritsa ntchito anthu tomwefe kupereka Uthenga wake kwa anthu anzathu. Tere lero Mulungu sakudzagwiritsa ntchito angelo kupereka Uthenga wachipulumutso ayi.

Mwanjira ina Uthenga ukunena kuti,tiyenera kuyanjanitsidwa kwa Iye ngati tingamvetsetse momwe Mulungu amachitira pakupereka chisomo cha chipulumutso kwa ife.

21. Koma ndidzakufotokonzeracholembedwa pa lemba la choonadi; ndipo palibe wina wakudzilimbikitsa pamodzi ndi ine, kutsutsana ndi aja, koma Mikaelikalonga wanu.

Tsono ndime iyi, ikugwirizana ndi ndime zina m'mbuyomo momwe muli nkhondo ya maufumu ena amene akulimbana ndi a Yuda.Koma chimene chiyenera kudziwika ndichakuti alipo akalonga oteteza Israeli, motsogozedwa ndi Kalonga Wamkulu, amene ndi Yesu Kristu. Kutanthauza kuti Kristu ndiye mwini mpingo kotero kuti amautetezera nthawi zonse pakutuma akalonga /angeloake.

Ndiye ndifuna titsirize ndi mau akuti mngelo akumuuza Danieli kuti ayenera kuona mau a Mulungu kuti ndiwo oona, kotero kuti sadzitsutsa ayi. Kutsindika kuti mau a Mulungu ndiwo chidachokhacho cha mwana wa Mulungu pamene akumenya nkhondo yauzimu. Mwachisoni kuti ena a ifesitikhoza kugwiritsa ntchito mau a Mulungu ngati chidachogonjetseramdani wathu.

Kwalerotilekeza pano ndipo timasanthula Danieli 10:10-21, m'mene timaunika za m'thengawa Kumwamba.

Ambuye akudalitseni inu.  Amen!